

# Chidule Cha Ntchito Zomwe A Bungwe La DFID Akhale Akugwira M'malawi Kuyambira Mchaka Cha 2011 mpaka 2015

May 2012

## Zifukwa Zimene DFID ikugwirira Ntchito Zake Ku Malawi

Malawi ndi dziko laling'ono limene lili kutali ndi nyanja kum'mwera kwa Africa. Dzikoli ndi limodzi la maiko osaukitsitsa lomwe lili pa nambala 153 pa maiko 169 poyerekezela kukwera kwa umoyo wa anthu. Chiwerengero cha anthu chikukwera ndipo chikuyembekezeka kufika 23 miliyoni pomafika chaka cha 2025. Pafupifupi anthu 40 pa 100 m'dzikoli akukhala pa umphawi. Dziko la Malawi likukwaniritsa zolinga zopititsa patsogolo chitukuko cha miyoyo ya anthu zotchedwa 'Malawi Development Goals(MDGS),' ndipo izi ndi kuchepetsa umphawi, njala, imfa za ana osapyolera zaka zisanu, kulimbana ndi kachilombo ka HIV komanso kuonetsetsa kuti anthu akumwa madzi abwino. Kusinthaku kukuchitika mwapang'onopang'ono, kotero kuti dzikoli lili ndi zofunika zambiri kuti litukuke. Imfa za amayi apakati zikuchitikabe, amayi apakati khumi amamwalira tsiku lililonse. Pafupifupi anthu mamiliyoni atatu akusowa madzi aukhondo. Nkhani zakusasiyanitsa pakati pa amuna ndi akazi zilipobe m'madera ambiri.

Pafupifupi gawo limodzi pa magawo atatu achuma chagona pa ulimi. Anthu pafupifupi 90 pa 100 ndi alimi ang'ono kapena okulirapo. Kukula kwa chiwerengero cha anthu, ndiponso kusintha kwa nyengo ndi zimene zikupangitsa kuti ulimi usachite bwino, zomwe zimapangitsa kusowa kwa chakudya. Ngakhale kuti m'mbuyomu chuma cha Malawi chimakwera, mzaka ziwiri zangothazi chatsika kwambiri, zimene zapangitsa kuti ntchito zamalonda ndi chuma m'makampani omwe si a boma zisamayende bwino. Kutichuma chiyambenso kuyenda bwino ndi kuti dziko la Malawi likhale lodzidalira palokha ndicho chinthu chofunika ndi choyenera kuyikidwa patsogolo. Mabungwe olimbikitsa ufulu wa demokalase nawonso ndi ofowoka.



Flora ndi mwana wake pa chipatala cha Balaka. Amayi ambiri masiku ano akubereka ku chipatala. "Ine ndinabereka mwana wangayu ndi madotolo odziwa bwino ntchito yawo. Kubereka tsopano sikovutanso ayi"



Ana a pulayimale ndi aphunzitsi awo ku Dedza. Pologalamu ya DFID iphunzitsa aphunzitsi ambiri, imanga sukulu zambiri kuti ana asamabwereze kapena kusiyira sukulu panjira, ndinso kuthandiza masukulu 5,500 onse a pulayimale pogwiritsa ntchito dongosolo latsopano la ndalama zopititsira patsogolo maphunziro.

Zolinga zathu ku dziko la Malawi ndi kuthandiza ndi kupititsa patsogolo ntchito za ulimi, kupatsa anthu mwayi woti adzipeza ndalama ndikukweza miyoyo yawo pa chuma, komanso kulimbikitsa za makampani omwe si aboma. Tidzapitilizanso kuonetsetsa kuti a Malawi akuthandizidwa pa ntchito zaumoyo, zamaphunziro, zamadzi ndi za ukhondo. Chithandizo chathu kumbali ya maphunziro chagona pa nambala ya ana mkalasi omwe akuyenera kuphunzitsidwa ndi mphunzitsi m'modzi kuchoka pa 80 mchaka cha 2010 kufika pa 60 mchaka cha 2013. Tidzaperekanso mwayi kwa nzika za Malawi kukhala ndi mwayi wowonetsetsa zomwe atsogoleri awo akuchita ndikuwafotokozera pomwe akuyenera kukhonzza komanso kuti adzitenga nawo mbali pa zochitika monga boma la demokalase. Tidzathandizanso atsikana ndi amayi kupeza mwayi wokwanira pantchito za chuma ndi zina zokhudza chitukuko cha dziko la Malawi.

## Chimene Tikufuna Kudzapindula

- Anthu 15,000 owonjezera apatsidwe ngongole
- Anthu 350,000 athandizidwe pa nthawi ya ngozi zogwa mwa dzidzidzi
- Amayi 113,600 abeleke mothandizidwa ndi achipatala odziwa bwino ntchito yawo
- Amayi owonjezera 22,000 athandizidwe kugwiritsa ntchito njira za makono zakulera
- Ana okwana 443,000 omwe 233,000 a iwo ndi atsikana athandizidwe kupita ku sukulu za pulayimare. Atsikana 15,000 alipilidwe ku sukulu za sekondale
- Anthu 750,000 owonjezereka apatsidwe madzi abwino
- Atsikana ndi amayi 406,900 apatsidwe chitetezo chokwanira ndipo apeze mwayi otengera milandu ku Polisi, ku makhoti ndi mabwalo ena onse mwachilungamo

## Amene Tidzagwira Nawo Ntchito

Tidzagwira ntchito ndi magulu amene ali oyenera kubweretsa zotsatira zaphindu pa chuma chogwiritsidwa ntchito. Mgwirizano wathu ndi maguluwa udzagona pamfundo zokhwima zomwe zidzafunika pokweza miyoyo ya a Malawi ndipo izi zikuphatikizapo magulu omwe amalemekeza ufulu wachibadwidwe, kupanga zinthu mosabisa komanso kagwiritsidwe kabwino ka ndalama. Tidzayesetsa kugwira ntchito limodzi ndi maguluwa pofuna kukwaniritsa cholinga chimodzi chopititsa patsogolo chitukuko. Ogwira nawo ntchito adzaphatikizapo boma la Malawi, mabugwe omwe si a boma (ma NGO ndi ma CSO), makampani omwe si a boma, akatswiri antchito zosiyanasiyana, mabugwe azakafukufuku ndi magulu ena.



Kupeza madzi abwino: Pulojekiti yobweretsa madzi aukhondo ya Kasumbu ndi Mpando yathandiza kupereka malo otungira madzi aukhondo okwana 326 yomwe ikuthandiza anthu pafupifupi 61, 500

## Momwe Tidzagwirire Ntchito

Kusiyana ndi kale lonse, komanso ndi m'mene chuma chikuyendera padakali pano, tili ndi ntchito yowonetsetsa kuti ndalama zikugwiritsidwa ntchito moyenera pa chilichonse chomwe tikupanga. Tidzawonetsetsa kuti pa chilichonse chimene tikupanga pakhale zotsatira zake, zinthu zisachitike mobisa ndipo ndalama zonse zagwiritsidwa ntchito ndikupindula moyenera. Mogwirizana ndi momwe eni ake odulidwa misonkhowo akufunira kuti ndalama zawo zigwirire ntchito pa chitukuko. Tidzakwaniritsa pochita izi:

- Kugwira ntchito ndi Boma la Malawi ndi magulu ena poonetsetsa kuti ndalama zikugwira ntchito yake moyenera ndipo zotsatira zake zikuwoneka pa ntchito zonse zikugwiridwa komanso palibe katangale wina aliyense akuchitika;
- Kuwonetsetsa kuti kupanga mapologalamu, kuwavomereza, kuwagwiritsa ntchito, kupanga kalondolondo ndi kuwunika kwa mapulogalamu onse ziyende ndi kuwonedwa mozama, mwadongosolo lake mkati ndi kunja kwa bungweli;
- Kukhazikitsa njira zomva kwa a Malawi pa mmene thandizo la ku UK likusinthira miyoyo yawo;
- Kuonetsetsa kuti mauthenga okhudza mapulojekiti awo ndi ndondomeko za kayendetsedwe ka ntchito zawo zikuwafikira anthu komanso ndi zolondola.

## Mukafuna Kudziwa Zambiri

Zambiri zokhuza mapulani antchito za ku Malawi chonde fufuzani pa intaneti [www.dfid.gov.uk/malawi](http://www.dfid.gov.uk/malawi) DFID Malawi, c/o British High Commission, Convention Drive, PO Box 30042, Lilongwe 3, Malawi General Enquiries: [enquiry@dfid.gov.uk](mailto:enquiry@dfid.gov.uk)

© Crown copyright 2012

Udindo wakukopera momwe zilembo ziliri ndi m'mene zasanjidwira komanso kawonekedwe ka zanenedwa mwambazi kali ndi eni ake amene atulutsa cholembedwa chino. Cholembedwa chino mutha kuchitulutsa m'mene chiliri kupatulapo Chizindikiro cha umwini chosonyeza DFID ndipo simudzalipitsidwa bola kungowonetsetsa kuti mwachitulutsa molondola ndi mosasocheretsa anthu. Nenaninso kuti cholemberachi eni ake ndi a DFID. Olemba ndi kusindikiza ndi a Department for International Development 2012